

Phunziro La Ziwanda

Dera Lathupi



Tsopano ine . . . ? . . . [Malo opanda kanthu pa tepi—Mkonzi]. Iyi ndi nthawi yoyamba yomwe ndinayamba ndachitapo izi mu misonkhano yanga chiyambireni kukhala ku munda. Iyi ndi nthawi yatsopano. M'bale Baxter anapita; ndipo—ndipo M'bale Bosworth ali ku India, kapena, Afrika; ndipo M'bale Baxter, sindikudziwa komwe iye ali. Iye anapita kwinakwake, ndipo ena onse a iwo achokapo ndipo apita. Ndipo Billy ndi ine tiri kuno tokha, chotero ife tikungokhala ndi nthawi yopambana: tikumangodzuka, kumapha ndi kumadya. Chotero, ife—ife tikukhala ngati tikumverera ngati kuti mwina ife tingakwanitse, mothandizidwa ndi Ambuye, tikhoza kumachititsa msonkhano mopitirira, tokha tokha. Ndi chifukwa chake ndine wokondwa kuziwona izo zikupitirira pang'ono, pa chifukwa chimodzi chimenecho. Ine ndikukhulupirira Ambuye atithandiza ife kuchita zimenezo. [Osonkhana akuti, "Ameni."—Mkonzi]. Tsopano, inu mukudziwa pali . . .

Ine ndimawakonda ondiyendetsera zinthu anga. Ndiri ndi abale ena okoma, Bosworth, Baxter, Lindsay, Moore, onse, alipo faivi a iwo, Baron von Blomberg. Iwo ndi amuna abwino kwambiri basi. Koma basi pamakhala chinachake, pamene ulibweretsa gulu la anthu pamodzi, wina amakhala ndi chinthu china, wina amakhala ndi china. Nthawizina zimakhala zotsemphana ndi chimene ine ndikuganiza inemwini. Chotero ine—ine—ine ndikumverera kuti ine ndamasuka tsopano. Ife tikhoza kungokhala ndi nthawi yopambana, kungopindira mikono ya malaya athu, ndi kungojoweramo ndi kumadya. Ine ndikuganiza zopindira malaya ako ndi kumakhala ndi—ndi nthawi yopambana.

Baibulo langa loyambirira linali chirengedwe. Ndinkamuphunzira Mulungu kudzera mu chirengedwe. Ndipo ine ndimakonda kuwedza. Momwe ine ndimakondera kuwedza! Ndipo iwe umakonda kuwedza, mwana wanga? Ngati iwe umakonda kuwedza, ndipo nkumawakonda amayi ako, iwe udzakhala mnyamata wabwino. Ndipo ngakhale kutembenuka kwanga sikunandichotsere ine zonsezo. Chotero tsiku lina ndinali uko kumapiri, ndimakawedza kumeneko. Tsopano, izi ndi zoti zimupindulire mnyamatayu. Ndipo ine ndinali kuwedza uko mmapiri . . . Ndi ana aang'ono enawo, ndithudi, amene akhala pozungulira. Ndipo ine ndinali kuwedza mphuta. Ndipo, oh, zimakhala zopambana mu nthawi ya kuphukira. Ine ndimapitirira chomwecho, ndipo panali mphuta

mu kadzenje kenako, inu mukudziwa, monga chomwecho. Ndipo ndimangowatamanda Ambuye ndi kukhala ndi nthawi yopambana, ndikufuula. Nthawizina, kumaponyera chingwe changa pansi. Ine ndimakhulupirira mu kufuula. Ameni. Ine ndithudi ndimatero. Chifukwa, ndimadziwa chinachake chandigwira ine, ndipo icho chimangochita chinachake kwa ine.

² Chotero ine ndinali nditapita pang'ono chabe m'mawa umenewo, ndipo pamene ndinabwerako, chinthu chachirendo kwambiri: Kuli zimbalangondo zambiri ku dziko la kumeneko, mu New Hampshire. Ndiri ndi msasa waung'ono kumeneko, kumene ndimakawedzako. Ndinali ndi tenti yanga yakale yaing'ono kumeneko, tenti yaying'ono yousirako yomwe ndakhala ndikukhalamo. Ndipo chimbalangondo chakuda ndi chinthu chosautsa kwambiri chomwe chiripo. Chotero, chimbalangondo chachikazi ndi tiana take tingapo ting'onoting'ono tinadzalowa m'menemo, ndipo tinadasokoneza mu tenti yanga!

³ Tsopano, kodi ukuganiza kuti ine ndikanatani nacho chimbalangondo chimenecho, mtsikana wamng'ono kumbuyo uko wa tsitsi lofiira limenelo, kumbuyo uko? Ine ndimayenera kuti ndichitsatire icho kwenikweni, sichoncho ine?

⁴ Koma izi ndi zomwe chinachita. Chinadzalowamo, chinadzang'ambira tenti yanga pansi ndipo chinamwazira panja chirichonse, ndipo chinadya chakudya changa chonse chimene ndinali nacho kumeneko, ndipo icho chimangomva bwino basi. Chotero pamene ine ndinadzabwera, icho chinadzachokapo. Ndipo chinafuulira kwa tiana take, ndipo kamwana kamodzi kakang'ono kanathawa naye. Ndipo winayo sakanathamanga; iye anangokhala pamenepo. Kananditembenuzira nsana wake, monga chonchi, ndipo iko kamachita chinachake. Ndipo ndinalibe chirichonse mdzanja langa koma kankhwangwa kakang'ono kammanja kakale. Ndinali ndikudula mitengo ikuluikulu ina kumeneko. Chabwino, iye anangothawira kutali, oh, ine ndikuganiza pa pholo la telefoni limenelo kunja uko, ndipo iye anakakhala pansi. Anafuulira kwa chimbalangondo chaching'ono chokalamba ichi, ndipo icho sichinapereke tcheru lirilonse kwa iye. Icho chinangokhalabe pamenepo.

⁵ Ine ndinaganiza, “Kodi kanthu kakang'onoko kameneko kakuchita chiyani?” Ndinapita moyandikirako pang'ono. Ndimawopa kuti ndiyandikire kwambiri, kuwopa kuti chikhoza kundikanda ine. Chotero ine—chotero ine—ine sindimawonapo mtengo, ndipo ndimadziwa kuti icho chikhoza kukwera nachonso. Chotero, ndipo sindimafuna kuchiyandikira kwambiri icho, chifukwa ine ndimachidziwa chikhalidwe cha chimbalangondo. Chotero, ndimapita moyandikirako pang'ono. Ndipo inu mukudziwa chimene chinadzachitika?

⁶ Tsopano, ine ndimakonda mapanikeki. Ndi angati a anyamata inu amene mumakonda mapanikeki? Oh, amwene! Oh, ine... Anyamata achikulire, nawonso. Ine ndawaona iwo akukwezanso manja awo. Tonsefe timakonda mapanikeki, ndipo ine ndimangowakonda iwo, ndipo ine ndimakonda kutsanulira uchi pa iwo. Pokhala wa Baptisti, mukudziwa, ndizo zimene zimatipangitsa kukhala owongoka, mukudziwa, ndi uchi, inu mukudziwa. Chotero, ndipo tamverani, ine sindimakonkha pa iwo, ine ndimazibatiza kwenikwensi izo. Ine ndimatsanulira kwenikweni pa iwo mpaka pomwe angakhale abwino kwenikweni ndi olemerera. Sindimangokonkha pang'ono apa ndi apo. Ine ndimatsanulira iwo kwenikweni pa iwo, ndimawakhutitsa onsewo ndi uchi.

⁷ Ndiyeno, inu mukudziwa, ine ndinali ndi ndowa ya uchi pamenepo, theka la galoni ya ndowa ya uchi. Ndipo zimbalangondo zimakonda kwambiri uchi. Chotero kanthu kakang'ono aka kanali katalowa mmenemo ndipo kanadzachotsa chivinikiro pa ndowa ya uchiyo, ndipo anali atakhala pamenepo monga chonchi, ndi ndowa yaing'ono iyi ya uchi mkhwapa mwake, monga *chonchi*. Iye anatenga... Ndipo iye samadziwa momwe angadyere, monga inu mumachitira, inu mukudziwa, chotero iye anadzangonyikamo mapazi ake aang'ono mmenemo ndi kumanyambita iwo monga *choncho*, ndi kumanyambita iwo. Ndipo anapotoloka kuti andiyang'ane ine, ndipo maso ake aang'ono akale onse anali atamatika pamodzi, mimba yake yaing'ono inali ikuterera mmene ikanathera, ndi uchi. Iye anali atangokhala pamenepo, akumatsitsira pansi dzanja lake ndi kumanyambita uchi, monga *choncho*, basi molimbika mmene iye akanathera.

⁸ Oh, mai, ine ndinaganizira za msonkhano wabwino wachikale wa Mzimu Woyera, pomwe ife tinkangoitsegula ndowayo, kulowetsa dzanja lathu pansi mu chidebecho ndi kumanyambitapo. Nkumangopitirirabe, inu mukudziwa, kumangonyambitapo.

⁹ Ndipo kodi inu mukudziwa chinthu chomwe chinali choseketsa, apobe? Kanthu kakang'ono ako katapeza zochulukuka zimene kakanakwanitsa, anaisiya ndowayo pansi ndi kumathamangira kumeneko. Inu mukudziwa chimene chinachitika? Mayi wa zimbalangondoyo ndi chimbalangondo china chaching'ono zinayamba kumunyambita iye, kumamuchotsapo uchiwo.

¹⁰ Chotero, chabwino, mwinamwake msonkhano wathuwu ukhala chinachake mwa dongosolo limenelo, ine ndikuyembekeza, kuti tikhoza kumakangowauza ena, ndipo ulemelero wa Mulungu nkumagwera pa ife. Chabwino.

¹¹ Ndine wokondwa kukuwonani inu ana aang'ono uko. Ine ndimakonda kukuuzani inu chinachake ngati chimenecho.

Ndipo mwinamwake mawa masana, ife tidzakhala ndi nthawi yochulukwa, ndipo—ndipo tikhoza kudzayankhula zochulukirapo pang’ono. Ndipo tiyankhule ndi adadi ndi amayi tsopano za chinachake.

¹² Ife tiyankhula pa *Phunziro La Ziwanda*. Mu Masalmo 103:1 mpaka 3, tiwerenga ndime izi. Pafupifupi mtumiki aliyense ndi m’busa, kapena wowerenga Baibulo, amawadziwa iwo pa mtima.

Lemekeza YEHOVA, O moyo wanga: ndi zonse zomwe ziri mwa ine, dalitsa dzina lake loyera.

Lemekeza YEHOVA, O moyo wanga, ndipo usaiwale zonse za zokoma zake:

Yemwe amakhululukira zonse za mphulupulu zako; yemwe amachiritsa nthenda zako zonse;

¹³ Ine ndikufuna kuti inu muzindikire pamenepo, zinali “zonse.” “Yemwe amakhululukira zonse za mphulupulu zako, Yemwe amachiritsa nthenda zako zonse.” Tsopano tingaweramtse mutu wathu kamphindi chabe.

¹⁴ Tsopano, Atate Akumwamba, ife tikukuthokozani Inu masana ano, chifukwa chodzakhala pano. Ife tikukuthokozani Inu chifukwa cha ana aang’ono awa omwe akhala apa, iwowo ndi amuna a mawa, ndi akazi, ngati kuli mawa, ngati Yesu achedwa. Ndipo tsopano, Atate, tikupemphera kuti—kuti Inu mutidalitse ife tsopano pamene tikuyankhula tsopano pa Mawu Anu, ndi zokhudza mdani wamkulu yemwe ife tiri naye, Satana. Ife tikupemphera, Mulungu, kuti Inu mutilole ife kuti tiyike asirikali patsogolo, gulu la makina apa, mphamvu ya Mulungu, omwe ati alimbane naye iye usikuuno mu kagawo kalikonse ka malo ake, Ambuye, ndi kumuwonetsa iye kuti alibe maufulu ovomerezeka aliwonse nkomwe, kuti Khristu anamugonjetsa iye mmalo mwathu apo pa Kalvare, pamene Iye anafa, ndipo Iye anawononga maulamuliro ndipo anamulanda Satana mphamvu iliyonse—iliyonse yomwe anali nayo. Ndipo, Mulungu, tipatseni ife nzeru ndi kumvetsetsa tsopano, kuti tikadziwe ndi kuti tikafotokoze kwa anthu momwe angachiritsidwire ndi momwe angamugonjetsere Satana. Mu Dzina la Yesu ife tikupemphera. Amen.

¹⁵ Tsopano kwa maminiti pang’ono ife tiyankhula pa *Phunziro La Ziwanda*. Inu mumamva zochuluka kwambiri za ziwanda. Tsopano, mawa masana ife mwinamwake tidzamalizitsa. Ine ndimafuna masiku awiri a sabata ino, mulimonse, kuti ndilalikire pa izi, basi. . . kapena masiku awiri pa misonkhano ya masana, kuti ndidzayankhule pa izi.

¹⁶ Tsopano, chinthu choyambirira, chimene chiwanda chiri. Inu mumamva anthu ambirimbiri akukamba za chiwanda. Chabwino, tsopano, “chiwanda, mdierekezi,” zonsezo zimachokera ku mawu amodzi, ndipo mu Chingerezi

amatchedwa “wozunza.” Munthu yemwe amazunza ndi mdierekezi, woyipayo. Iye amati. . .Tsopano, Baibulo lero, kwa ochuluka, kwa anthu ambiri, ndi bukhu linalake lachikale la mmbuyo limene agogo aamuna ndi agogo aakazi ankaliwerenga, kapena chinachake monga chimenecho. “Palibepo zochuluka kwa ilo, ilo ndi la anthu okalamba, ndi zina zotero.” Koma uko nkulakwitsa. Ilo ndi la aliyense. Ndipo ziwanda ndi zozunza zimene zimatizunza ife.

¹⁷ Tsopano, pali ziwanda zimene zimabwera mu solo ya munthu, ndipo izo zimakhala, mu manenedwe, omwe angakhale—omwe angakhale mu. . .Ine ndinganene ichi, ngakhale, chiwanda chimene chimabwera mu solo ndi chinachake chomwe chimazunza solo.

¹⁸ Nthawi zambiri inu mukhoza kumuwona munthu mwinamwake wamisala. Tsopano, iwo mwinamwake akhoza kukhala munthu wotembenuka, wozadzidwa ndi Mzimu Woyera, ndipo komabe nkukhala wamisala motheratu. Mukuona? Uko nkulondola. Izo sizimakhala ndi chochita chirichonse ndi solo. Ndi wozunzayo, mwaona, chinachake chomwe chimawazunza iwo.

¹⁹ Tsopano, nthenda zonse, tikuyenera tipeze kaye poyamba kuti nthenda zonse zinachokera kwa mdierekezi. Mulungu si woyambitsa wa nthenda. Palibe nthenda yomwe imachokera kwa Mulungu. Mulungu nthawizina amamulola Satana kuti ayike nthenda pa inu, ngati chikwapu chokubwezeretserani inu ku nyumba ya Mulungu, pamene inu simunamvere. Koma nthenda, mu chiyambi chake, imachokera kwa mdierekezi. Kodi inu mungaganizire kuti munthu angakhulupirire kuti Mulungu, Atate athu Akumwamba, angakhale woyambitsa wa chinthu ngati nthenda ndi imfa? Chabwino, ayi, Iye siali, sanateropo nkomwe, sadzateropo. Mulungu amailola imfa chifukwa cha kusamvera. Mulungu amailola imfa. Monga wolemba wina ananenera, “Zonse zimene imfa ingachite, Mulungu amazikonza izo kukhala chikwere ndipo chimatikokera ife mu Kukhalapo kwa Mulungu, wokhulupirira.” Koma mawu akuti *imfa* amatanthauza “kulekanitsidwa.”

²⁰ Yesu anati, “Iye amene amva Mawu Anga ndi kukhulupirira pa Iye amene anandituma Ine, ali nawo Moyo wosatha.” Ndipo Iye anati, “Ine ndine chiukitsiro, Moyo, iye amene akhulupirira mwa Ine, angakhale amwalire, komabe adzakhala moyo, ndipo aliyense amene akhala moyo nakhulupirira mwa Ine sadzafa konse.” Ndipo ife timanyamula matupi a wina ndi mzake kupita nawo kwa woyang’anira wa manda athu. “Koma iye sadzafa konse.”

²¹ Tsopano ngati mungawone pamene Iye ankayankhula za Lazaro, Iye anati, “Lazaro akugona.”

22 Ophunzira, anthu onga momwe ife tiriri, anati, “Oh, ngati iye akugona akuchita bwino.” “Iye ankanthauza kupumula,” zomwe iwo ankaganiza.

23 Koma Iye anabwera ndipo anadzawayankhula iwo mu chinenero chawo. Iye anati, “‘Iye wafa,’ zomwe inu mumakhulupirira. Koma,” anati, “Ine ndikupita ndikamudzutse iye, ndikamudzutse iye.” Mukuona? Mukuona? Pamene inu . . .

24 *Imfa* imatanthauza “kulekana.” Tsopano, ngati wina wa inu angati, mmodzi wa m’banja mwanu akafa, kapena chinachake, iye ndi, ngati ndi wotembenuka mtima, iwo sanafe. Iwo afa mu kamvetsedwe ka umunthu. Koma iwo angolekanitsidwa chabe ndi ife, koma iwo ali mu Kukhalapo kwa Mulungu. Iwo sanafe, ndipo iwo sangakhoze kufa, ndi zosatheka kuti iwo angafe. Yesu anati, “Iye amene amva Mawu Anga nakhulupirira pa Iye yemwe anandituma Ine ali nawo Moyo wosatha, ndipo sadzabwera ku chiweruzo, koma wadutsa kuchoka ku imfa wapita ku Moyo.” Chotero, iye sangafe. Chirichonse chimene chiri cha chisavundi, Chamuyaya, sichingawonongeke. Iwo ndi Moyo wosawonongeka. Iye alinawo Iwo chifukwa Mulungu waupereka Iwo kwa iye. Ndipo osati—osati mwakugwirira ntchito; izo ndi zokhala . . . Izo ndi zopanda mangawa. Mulungu amaupereka Iwo kwa iye.

25 Mulungu amaitana. Palibe munthu angadze kwa Mulungu pokhapokha Mulungu atamuitana iye. Yesu anati, “Palibe munthu angadze kwa Ine pokhapokha Atate Anga atamuitana iye, atamukoka iye.” Nkulondola uko? Chotero ndi Mulungu mu zonsezo. Mwinamwake mawa masana tidzatenga zochulukirapo pang’ono chabe za zimenezo, chifukwa ine ndikufuna ndichipereke chinthu ichi cha *matenda*, kwa inu, kuti inu muthe kuchiwona icho.

26 Inalipo nthawi imene ife tinaphuka mwa agogo a agogo athu. Inu mukudziwa zimenezo. Adokotala amadziwa zimenezo. Chabwino, inu mumatero, nanunso, inu owerenga Baibulo. Inu mumadziwa nyongolosi ya moyo inayambira mwa agogo a agogo anu, kuyamba kukhala nyongolosi, ndipo inatulukira kudzera mwa agogo anu aamuna, kenako kudzalowa mwa abambo anu, kenako kwa amayi anu ndi pamene inu muli tsopano. Uko nkulondola. Ngakhale Lemba limaphunzitsa zimenezo. Lemba lake ndi ili kwa inu ngati mukufuna. Ine ndikukhulupirira linanena kuti Levi anapereka zakhumi pamene iye anali mchiuno mwa Abrahamu, yemwe anali agogo a agogo ake aamuna. Nkulondola uko? Chotero, mwaona, nyongolosi inayambira kumbuyo uko.

27 Koma ma solo anu anapangidwa maziko a dziko lapansi asanakhalepo, pamene Mulungu anamulenga munthu mu chifanizo Chake Chomwe; mzimu wa munthu; osati *ka* munthu mu chifanizo Chake Chomwe, koma *munthu* mu chifanizo Chake

Chomwe. Mukuona? Ndiyeno Iye anawapanga iwo mwamuna ndi mkazi, Iye asanakhale konse ndi munthu mu fumbi la dziko lapansi. Ndikanakonda tikanakhala ndi mpata masana ano, nkutenga nthawi yathu ndi kubwerera mu zimenezo. Kungowona momwe Mulungu. . . Tsopano, izo mzapakati pa mzere, koma, pamene muziwona, izo zimabwera pomwepo ndi mzere. Mukuona? Momwe kuti Mulungu, kumbuyo uko ku chiyambi, chimene Iye anachita kumeneko, ndi momwe Iye anasunthira mpaka mu dziko lapansi ndi momwe Iye anamupangira munthu mchifanizo Chake; ndipo kenako Mulungu anadzapotoloka ndipo anadzapangidwa mchifanizo cha munthu, kuti adzamuwombole munthu.

²⁸ Tsopano, pamene Mulungu anamupanga munthu mu chifanizo Chake, iye anali munthu wa mzimu. Ndipo kenako panalibe munthu woti azilima nthaka. Ndiye Iye anamulenga munthu kuchokera mu fumbi la mnthaka. Tsopano, ofukula zapansi, ndi ena otero, ndi anthu awa omwe amafufuza ndi kumapeza mafupa akale, ndi zina zotero, ndi kumakhulupirira mu kusintha. . . Ine ndimakhulupirira mu mtundu wolondola wa kusintha. Munthu amasintha kuchokera kwa iyemwini, koma osati onse kuchokera ku kakhungu kamodzi. Ayi, bwana, chifukwa m—mbalame yakhala ili mbalame chiyambire pomwe Mulungu anailenga iyo kukhala mbalame, ndipo nyani wakhala ali nyani, munthu wakhala ali munthu. Uko nkulondola.

²⁹ Tsopano, ndinali kuyankhulana ndi dokotala kuno kanthawi mmbuyo, mu Louisville. Iye anati, “Bwanji, M’busa Branham!” Ine ndinali kuyankhula za momwe mzika zaku Afrika, momwe iwo amadyera, basi amangopita pamenepo. . . Oh, zina za zinthu zowopsya kwambiri zimene inu munayamba mwaziwonapo, momwe iwo amakhoza kudyera! Amangotola zinthu zomwe zavunda, ziri ndi mphutsi mmenemo, amangozisa izo, mphutsi ndi zonse. Sizipanga kusiyana kulikonse kwa iye. Mukuona? Iwo anati. . . Amamwa chirichonse, sizimapanga kusiyana kalikonse zomwe izo ziri. Iye anati, “Koma, M’busa Branham, anthu amenewo si anthu.”

Ine ndinati, “Oh, inde, iwo ali. Iwo ndithudi ndi anthu.”

³⁰ Ine ndinati, “Chinthu choyandikana kwambiri ndi munthu, mu mzere wa zinyama, ndi chimpazi. Ndipo inu mwayesetsa kwa zaka foro sauzande kuti mupeze liwu limodzi kuchokera kwa chimpazi, koma iye sangachite zimenezo.” Ine ndinati, “chifukwa iye sangaganize. Iye alibe chirichonse choti angaganizire nacho.” Oh, inu mukhoza kumuphunzitsa iye zinthu zing’onozing’ono monga kavalo, gii ndi hoo, kapena kuvala magalasi, kapena kusuta ndudu, kapena kudziyimitsa yekha pa njinga, kukwera kavalo, kapena chinachake chonga zimenezo, koma basi monga “gii” ndi “hoo” kwa kavalo, kapena “whiiti” kwa galu, kapena chinachake ngati icho. Ine ndinati, “Iye ndi chinyama.”

³¹ “Koma mundilole ine ndibwerere ku Afrika, kwa mtundu wa mthengo kwambiri womwe iwo ali nawo, ndipo ndiwo mtundu waung’ono wa anthu aku tchire.” Ndipo ine ndinati, “Mwinamwake agogo-agogo-agogo-agogo-agogo ake aamuna sanamuwonepo konse mzungu kapena chirichonse. Chinthu chokhacho chimene iye amachidziwa, iye samadziwa nkomwe dzanja lamanja ndi lamanzere. Chinthu chokhacho chimene iye amachidziwa ndi kudya, ndipo iye amadya chirichonse chimene iye wachiyeza, kaya ndi thupi la munthu, china chirichonse, sizimapanga kusiyana kulikonse kwa iye, bola iye adye. Koma mundilole ndimutenge iye ali ndi zaka faivi zakubadwa, ndipo akamafika usinkhu wa zaka fiftini iye adzakhala akuyankhula Chizungu chabwino ndipo akhala ndi maphunziro abwino. Chifukwa chiyani? Iye ali ndi solo. Mulungu anamupanga iye kukhala munthu, ndipo amangokhala ndi ufulu womwewo basi kuti amve Uthenga, kamodzi kokha, monga ife timachitira kulalikira kuno, konsekonse mu Amerika, kwa anthu, mobwereza mobwereza ndi mobwereza, ndi kumawapempha, kuwachonderera ndi chirichonse. Mumulole iye awumve iwo kamodzi, ndipo mudzamuwone iye akufuula ndi kumathamangira ku guwa mwamsanga kwenikweni.” Mukuona? Inde, bwana!

³² Ndi chimene mtima wanga ukufuna, m’bale, lero, pamene ine ndiganiza za Afrika, ndi manja osauka aang’ono akuda aja mmwamba, akuti, “M’bale Branham, kamodzinso za Yesu!” Oh, chifundo! Pali chinachake mwa ine chimene chimakumba ndi kumatentha. Basi mwamsanga ndikapeza ndalama zokwanira, ndizipita kumeneko, aponso. Ndi zomwe ine ndimachita ndi ndalama iliyonse imene ine ndimaipeza, iliyonse, Mulungu amadziwa, kupatula zomwe ine ndimadyera. Ndipo anthu ambiri amandipatsa ine zovala zanga. Ndipo basi zomwe ine ndikhoza kumadyera, inemwini, basi zimene ine ndingazipeze, ine ndimaziponyera izo mu thumba la umishonare lomwe boma linakonza. Ine sindimalipira nkomwe msonkho pa izo. Ndimatengapo firi kapena foro, madolla faivi sauzande, ndipo ndimapita nazo kutsidya uko ndi kukalalikira Uthenga kwa anthu amene ine ndikudziwa kuti pa tsiku limenelo ine ndidzayenera ndidzayankhire. Ndipo ine ndidzadziwa chimene ndikuchiyankhira.

³³ Ine ndinkakonda kuteru, pamene ndipita mu mzinda, ine ndinkakhoza kukhala ndi msonkhano waukulu pamene iwo akhala ndi ndalama zambiri, ndipo amakhala ndi misonkhano yaikulu ndi masauzande a madolla, ine ndinkazipereka izo ku Red Cross ndi ena otero. Tsopano, tsopano, osati kuwaipitsa iwo, koma kumabwera kumeneko pa msewu atakwera galimoto ya madolla foro sauzande, yokhala ndi zingerengere zazikulu za dayamondi, akusuta ndudu, ndi madolla faivi handiredi pa sabata pa ndalama zimene anthu odwa-...Ayi, bwana!

Ayi, ndithudi! Ndipo pa izi, mwamsanga ukangotuluka mu mzindawo, iwo amati, “oyera odzigudubuza,” ndi chirichonse monga choncho, ndi kumanyoza, ndi kumachepsya chipembedzo chimene ife tikuchiimirachi. Ayi, bwana!

³⁴ Ine ndimatenga izo ndekha, ndi pamaso pa Mulungu ngati Woweruza wanga, ine ndimakaziika izo mu ntchito ya Uthenga uko, chotero ine ndimadziwa kuti pa Tsiku limenelo kuti ine ndidzatero... pamene ndidzayenera kuti ndidzayankhire za udindo wanga, ndizidzalankhula molondola. Ndizo ndendende kulondola, chifukwa ine ndikuzindikira kuti mmene ndikumasamalira anthu ine ndikumusamalira Mulungu. Mmene ndikuchitira ndi inu ndi mmene ndikuchitira ndi Khristu. Ndipo mmene mukuchitira ndi ine ndi chinthu chomwecho, uko nkulondola, ndi Khristu.

³⁵ Tsopano, kuwawona anthu monga chomwecho, ndi kuwona momwe munthu, ndiye, wokhala ndi solo ya chisavundi tsopano, imene siingafe, siingawonongeke, siingachite chirichonse koma kukhala ndi Moyo wosatha, umene Mulungu mwa payekha, mu chifuniro Chake Chomwe, anawupereka iwo kwa inu. Ndipo tsopano, ndiye, tsopano ine...

³⁶ Mundilole ine ndichikonze ichi pang’ono pokha chabe, kapena ndinene chinachake. Winawake achokapo ndipo azikati, “M’bale Branham ndi wa Chikalvanisti.” Ayi, ine sindiri. Ndine wa Chikalvinisti bola ngati Chikalvinisti chiri mu Baibulo. Koma pamene Chikalvinisti chichokamo mu Baibulo, ndiye ndine wa Arminian, mwaona. Ine ndimakhulupirira mu chiyero ndipo ndimakhulupirira mu Chikalvanisti, aponso. Koma, ziwiri zonsezo, china chinathamangira pa nthambi ndipo chinapita njira *iyi*, ndipo china chinathamangira pa nthambi ndipo chinapita njira *iyi*. Chikanapanda Bukhu la Aefeso, kuti linazibwezeretsanso izo ndi kudzaziika izo pamalo olondola pomwe Mulungu anaziika, ife tonse tikanasokonezeka. Koma awiri onsewo ali ndi chiphunzitso, koma akuyenera kuti azikike pa icho, aliyense, amenewo ndi a chiyero ndi a Chikalvinisti nawonso, Achiarminian. Tsopano, a Chikalvinisti ali ndi chinachake choona. Ine ndikukhulupirira zimenezo, kuti chiphunzitso cha Chikalvinisti...

³⁷ Ine ndimakhulupirira izi. Mu chitetezero, ine ndimakhulupirira kuti Mpingo uli ndi Chitetezero Chamuyaya. Wowerenga aliyense wa Baibulo amadziwa zimenezo, chifukwa Mulungu anazinena kale kuti Iwo udzawonekera kumeneko wopanda chilema. Nkulondola uko? Ndiye, Iwo udzakakhala kumeneko. Nkulondola uko? Bai... Mpingo ndi wotetezedwa Mwamuyaya. Tsopano, kodi inu muli mu Mpingowo, ndicho chinthu chotsatira. Ngati inu muli mu Mpingo, chabwino, ndinu otetezeka ndi Mpingowo, koma ndi bwino mukhalebe mu Mpingo. Ndipo kodi inu mumalowa chotani mu Mpingo? Pogwirana chanza? Ayi. Kulemba dzina lanu mu bukhu? Ayi,

bwana. “Mwa Mzimu umodzi ife tonse timabatizidwira mu Thupi limodzi.” Ndipo Thupi limenelo, Mulungu analiweruza pa Kalvare, linali Thupi la Yesu Khristu, ndipo ife timabatizidwira kulowa mu Thupi limenelo mwa Mzimu umodzi. Ife timakhala ndi Chitetezo Chamuyaya bola ngati ife tiri mu Thupi la Khristu, palibe chimene chingatilekanitse ife, palibe chimene chingatikhudze ife. Ngati iwe ungatulukemo, utulukamo mwa kufuna kwako kwako. Koma motsimikiza basi, ngati iwe uli mu Thupi la Khristu, motsimikiza basi monga momwe Yesu anaukira kwa akufa, inu mudzauka nanunso. Mulungu anachita kale zimenezo. Iye . . .

³⁸ Iwe sungachimwe. Oh, inu mumachita. . . Ine ndikhoza kukhala wochimwa nkuwona kwanu, koma ngati ine ndiri mwa Khristu, Mulungu samaziwona izo, chifukwa machimo ake amatetezera. . . Magazi Ake amatetezera machimo anga pamenepo. Mukuona? Ine sindingachimwe. “Iye amene wabadwa mwa Mulungu samachita tchimo, pakuti iye sangathe kuchimwa. Mbewu ya Mulungu imakhalabe mwa iye.” Mukuona? Iye, iye amafuna kutero, ngati iye alakawitsa, ndithudi, iye pomwepo amafuna kuti alape izo. Ngati iye ali Mkhristu weniweni, iye achita zimenezo. Ngati achisunga icho, iye amawonetsera kuti iye alibe chirichonse, kuyamba ndi kuyamba. Uko nkulondola. Iye alibe chirichonse, kuyamba ndi kuyamba. Koma ngati iye ali Mkhristu weniweni. . .

³⁹ Pomwe apa, inu mukadzala mbewu ya tirigu mu nthaka, iyo nthawizonse izikhala mbewu ya tirigu. Chisoso chikhoza kumuzungulira iye, ndi china chirichonse, koma ikhalabe mbewu ya tirigu ngati iyo ikuyimabe. Nkulondola uko? Ndipo ngati munthu wabadwa kwenikweni mwa Mzimu wa Mulungu, iye samalowa ndi kutuluka, ndi kubwerera mmbuyo ndi kupita mtsogolo, ndi kupita kunja mdziko ndi kudzabwereranso kuno. Ayi, bwana. Ayi, ayi. Sumakhala chisoso tsiku lina ndi mbewu ya tirigu tsiku lotsatira. Mulungu alibe zimenezo mmunda. Inde, bwana. Ngati iwe wabadwa mwa Mzimu wa Mulungu, ndiwe Mkhristu kuyambira nthawi imeneyo mpakana. . . mpaka iwe udzachokepo, ndipo zikatero ndiwe—ndiwe wachisavundi, ndi Mulungu. Uko nkulondola, ngati iwe uli mu Mpingowo.

⁴⁰ Tsopano, tsopano tiyeni tikambe za mbali ya imfa. Tsopano, zingatatheke bwanji munthu mu kachitidwe kameneko, mu chikhalidwe choterocho, kuti angadwale? Chifukwa chakuti thupi lanu silinawomboledwebe. Thupi lanu silinawomboledwe. Ziribe kanthu ndi motani, mmene inu muliri wabwino, ndi mmene muliri woyera, ndi mmene muliri wopatulika, ndi Mzimu Woyera wochuluka motani, iyo ndi solo yanu yokha. Ndipo solo yanu siinakwanirebe. Iyo yangokhala ndi M’dalitso, lonjezo la Mulungu, lomwe liri chikole cha chipulumutso chatu. Koma tsopano ngati ife tiribe chikole cha chiukitsiro chatu, tiribe machiritso Auzimu, ndiye ine sindidzakhala ndi chitsimikiziro

kapena chirichonse choti chinditsimikizire ine kuti chiukitsiro chiripo.

⁴¹ Chimodzimidzi ngati Khristu sakukhala mu mtima mwanga, ngati ine ndingazitenge izo kuchokera ku mtundu wina wa—wa chinthu cha mmalingaliro kumbuyo uko, ndikuyenera kukhulupirira kwinakwake monga chomwecho, chabwino, ndiye ine—ine—ine ndingakhale wokaikira pang’ono ndi izo. Ndipo ndicho chifukwa chake, uko ku Afrika, pamene iwo akamabwera, apa pamabwera mamishonare, amabwera ndi masauzande a mzika zimenezo, ndipo iwo anali atanyamula timafano tating’ono takale tadongo ndi chirichonse, ndi chifukwa chakuti iwo anali atangomva gawo la malingaliro la Baibulo. Uko nkulondola. Ndipo mpingo wanga womwe ndi wa Baptisti, Methodisti, Presbateria, onse amene amapita kumeneko. Koma pamene iwo anawona mphamvu ya Mulungu itabwera mu chiwonetsero, zimenezo zinakhazikitsa izo, iwo anadziwa pamenepo kuti Mulungu anali Mulungu.

⁴² Koma, tsopano, nchiyani chimayambitsa matenda awa? Tsopano, chinthu choyamba, iwo umakhala mzimu asanakhale matenda, chimodzimidzi basi monga inu munali mzimu inu musanakhale munthu. Tsopano ine ndimutenga M’bale Willett apa ngati chitsanzo. M’bale Willett, ine... Inalipo nthawi imene iwe ndi ine sitinali kanthu. Ndipo kenako chinthu choyamba, Mulungu anatipatsa ife moyo. Ndipo tiyeni titenge, tinene, ngati ine ndingalitengere thupi lanu pansi masana ano, inu munapangidwa ndi mulu wa timakhungu, titagwirana pamodzi ndi ma atomu. Ndipo tsopano, tsiku lina ma atomu amenewo adzawonongedwa, ngati Yesu achedwa. Inu mudzabwerera mmbuyo. Iwo adzangokhala monga momwe iwo analiri pachiyambi, kubwerera mu mpweya. Koma pamene mzimu wanu udzabwerera, ma atomu amenewo adzasonkhana pamodzi kenanso ndi mzimu umenewu ndipo adzabweretsapo M’bale Willett wina wofanana ndi ameneyo, adzangokhala wamng’ono, pamene iye anali pachimake chake.

⁴³ Pamene munthu wafika podutsa usinkhu wa zaka twente-faivi zakubadwa, iye amapeza makwinya angapo pansi pa maso ake, ndipo tsitsi lina la imvi limabwerapo. Izo zidzakhala, chifukwa imfa ikukutsatirani inu. Ndipo limodzi la masiku awa iyo idzakutangani inu. Ziribe kanthu kaya ndinu ndani, iyo idzakutangani inu. Koma pang’onopang’ono... Inu mudzafika pa ngodya apa, ndipo Mulungu adzakuchotsanipo pa ngodya imeneyo, ndipo inu mudzafika pa ngodya iyi *apa*, imfa idzatsala pang’ono kukutangani inu, ndipo kuno, koma pakapita kanthawi iyo idzakupezani inu. Komano, chimene imfa ingachite, iyo imakufikirani mwathunthu, ndipo kenako pa... pamene iyo yachita zonse zimene iyo ingachite... Pamene Mulungu anakupatsani inu moyo uwu, ndipo inu munali pachimake panu, pafupifupi pa twente-firii, pamene mudzafike

mu chiukitsiro inu mudzabwereranso ndendende basi monga momwe inu munaliri pamene inu munali wausinkhu wa zaka twente-firii, twente-faivi, imfa isanalowemo. Imfa idzachita chirichonse chimene iyo ingakhoze kuchita. Iyo inaikidwa mmenemo, koma inu mudzabwererako mmene munaliri.

⁴⁴ Tsopano, ngati lirilonse la anu—makhungu anu mu thupi lanu, tiyeni titsike nazo izo tsopano, inu mubwere khungu pa khungu, khungu pa khungu, ndipo mudzawaike iwo apa pa nsanja, khungu lirilonse la mthupi mwanu, inu mudzafika ku kanyongolosi kamodzi kakang'ono kumene inu munayambira, iko sikangawoneke ndi diso lachirengedwe. Inu mudzayenera kuyang'ana pogwiritsa ntchito magalasi owunikira. Ine ndinawonapo nyongolosi ya moyo pa galasi lowunikira. Iyo imawoneka ngati kaulusi kakang'ono kwambiri. Ndipo chinthu choyambirira chimene chimayamba ndi mu nsana mwenimwenimo, zimakhala ngati ka mfundo kakang'ono. Ndiko kakhungu kakang'ono koyambirira kamene kamabwera pamwamba pa khungu.

⁴⁵ Tsopano, ngati ndikanati nditenge kakhungu kamodzi kakang'ono kamene aliyense wa inu munachokerako, kakhungu kamodzi kakang'ono, nyongolosi... Kodi nyongolosi ndi chiyani? Nyongolosi ndi kanthu kakang'ono kwambiri, kochepetsa ka khungu. Chabwino, nchiyani chotsatira pamenepo? Tsopano, ndakutengerani inu pansu ku chidutswa chirichonse cha inu, kutsika kupita ku kakhungu kamodzi kakang'ono aka, ndipo ine sindinakupezenibe inu. Ine ndangopeza timakhungu tanu titayalidwa. Chabwino, ndiye, chinthu chotsatira, makhungu a magazi, ndi makhungu a mnofu, ndi chirichonse chimene izo ziri, kuziyala izo zonse kunjya uko, koma ine sindinakupezenibe inu. Tsopano, ine ndatsala ndi kanyongolosi kamodzi tsopano. Chabwino, ine nding'amba kakhungu kameneko. Tsopano, inu muli pati? Moyo wanu. Ndipo moyo umapanga kakhungu koyamba, kamene kali kanyongolosi, kenako chirichonse monga mwa khalidwe lake; galu amatengera galu, mbalame imatengera mbalame, munthu amatengera munthu. Kumawumba makhungu, khungu pa khungu, khungu pa khungu, zimakwera kufika pamene inu muli, munthu, kuwumbika kwa makhungu. Tsopano, zimenezo zinazodzedweratu ndi Mulungu kuti zidzakhala chomwecho.

⁴⁶ Koma, tsopano, nanga bwanji khansa? Tiyeni tikambe za iyo pang'ono pokha. Tsopano, Mulungu anakupatsani inu moyo wanu. Ndipo tinene kuti, ndi inu apa lero, ndi ine apa, pali—palibe chirichonse mdzanja langa, koma zikhoza kukhala kuti panali khansa pa nkono wanga nthawiyina. Chabwino, khansa imeneyo inafikapo bwanji pamenepo? Tiyeni tiwone chimene khansa imeneyo ili, tsopano tiyeni tiyiphwasule iyo, tiyeni tipite tikayitenge iyo. Tsopano, iyo ndi mulu wa timakhungu, nayonso. Kodi inu mumadziwa zimenezo? Chotupa,

ng'ala, chirichonse cha zinthu zimenezo ndi makhungu. Izo ziribe mawonekedwe ayi. Zina za izo zimayenderera, ndipo zina zimawoneka ngati kangaude, ndipo zina zimawoneka . . . zimayenda mtimizere, khansa yofiira, monga ngati timaulusi tatitali tofiira tikuyenderera mmenemo . . . Ndiyeno pali khansa ya duwa imene kawirikawiri imabwera pa bere la mkazi, imakhala ngati mapanikeki ataikidwa pa imzake, ndipo kenako iwo amayamba kumwazikanapo. Ndipo iwo amangomera paliponse.

⁴⁷ Nthawizina zophuka zimakhala zosiyana makulidwe, mbali *iyi*, yaitali, yotambalala, ndi chirichonse. Izo sizimakhala ndi mawonekedwe, chifukwa izo zimatengera mzimu womwe ulibenso mawonekedwe. Koma ndi kuchulukana kwa makhungu. Ndi mulu wa makhungu amene, tinene kuti, mwa inu tsopano muli chotupa kapena khansa, ndi kuwumbika kwa makhungu, akukula, akukula, akukula. Iwo akukudyani, akuyamwa moyo wanu kuchokera mwa inu. Iwo akukhalira moyo mpita wa magazi. Ng'ala imachotsa mamina a mu diso ndipo imakula pamwamba pa iwo, imadziphimba yokha, nkutsekeratu maso anu. Zina za izo zimabwera ndipo sizimafikira nkomwe . . . monga chifuwa chachikulu, chimene chimabwera mu kanyongolosi kakang'ono. Palibe chirichonse chimene chimakhala usinkhu wa izo. Kukula komweko kwa kanyongolosi kumapanga njovu, kumapanga nthā—nthata. Mukuona? Usinkhu wa nyongolosi ulibe kanthu.

⁴⁸ Ndipo zina za izo zimatenga mawonekedwe a thupi, zina sizitero nkomwe. Ndipo zina sizimapita konse mu makhungu. Zina zimakhala mzimu, kumazunza solo. Ife tiyesetsa kuti titenge gawo limenelo, gawo limenelo ndilisiira masana, ngati ndingathe, kumene kumachokera mzimu wa solo umenewo, ndi momwe zimatsikira pansu *apa*.

⁴⁹ Ndipo tsopano, abwenzi, ine sindikunena izi kuchokera ku zinazake zonga kuwerenga maganizo. Ine ndachitapo ndi ziwanda kwa zaka, ndipo inu mukudziwa zimenezo. Ngati inu mukanangodziwa chinthucho, misonkhano ikangoti yatha usiku, zomwe zimachitika nthawizina. Inu simukudziwa. Kumbukirani, pamene iwe ulimbana ndi mzimu, iwe umayenera kukhala kuti ukudziwa chimene ukuchikamba. Usangoyima pamene ndi kumapitirira, chifukwa sizikuchitira iwe ubwino uliwonse. Koma kwenikweni pamene chiwanda chiri chakuti chikumvera iwe, icho chimazindikira izo. Izo si momwe umakuwira mokweza, si kuchuluka kwa mafuta amene iwe umadzola. Ndi chimene chiri kumbuyo kuno chimene icho chingazindikire, Choonadi. Yesu anangonena kwa icho, “Tuluka.”

⁵⁰ Kumbukirani, ophunzira anakhala akumenya ndi kupinda, ndi kuyesetsa kuti achitulutse icho, ndi chirichonse. Iwo anati, “Nchifukwa chiyani ife sitinathe kuzitulutsa izo?”

Anati, “Chifukwa cha kusakhulupirira kwanu.”

⁵¹ Anati, “Tuluka mwa iye.” Mnyamatayo anadzagwa ndipo anakhala ndi khunyu lamphamvu limene sanayamba wakhlapo nalo. Mukuona? Mukuona? Izo zimazindikira ulamuliro.

⁵² Tawaonani anyamata amenewo kumusi uko, oyendayenda aja amene anamuwona Paulo akutulutsa ziwanda. Iwo anati, “Ife tikhoza kuchita chinthu chomwecho,” ana a wansembe wina. Chotero iwo anatsikirako ndipo anati, “Ife tikhoza kutulutsa ziwanda.” Machitidwe 19. Iwo anapita kwa munthu amene ankagwa khunyu, ndipo anati, “Ife tikukulamulira iwe, mwa Yesu. Tuluka mwa iye . . .” Mdierekezi anati, “Tsopano . . .” “. . . mu Dzina la Yesu, yemwe Paulo amamulalikira!”

⁵³ Mdierekezi anati, “Tsopano, ine ndikumudziwa Yesu ndipo ndikumudziwa Paulo, koma iwe ndi ndani?” Mukudziwa chimene chinachitika. Analumphira pa munthuyo, anang’amba zovala zawo, ndipo anakhala ndi khunyulo iwoeni, ndipo anathamangira ku msewu.

⁵⁴ Ziwanda zomwe zomwezo ziripo lero, chotero pali zotengeka zochuluka. Uwu ndi mpingo, madzulo ano. Pali zotengeka zambiri mdziko lero, zotchedwa machiritso Auzimu, zimene zikuyenera kuletsedwa. Izo ndi zimene zimabweretsa chitonzo pa Cholinga chenichenicho. Ndi chifukwa chake mumakhala ndi kulimbana kovuta kotereku. Pali zinthu zochuluka zotchedwa chipembedzo, lero, zimene zikuyenera kuletsedwa. [Malo opanda kanthu pa tepi—Mkonzi]. Sikanthu koma tizikhulupiriro! Ndi zimene zikupangitsa Mpingo woona wa Mulungu kuti uzivutika kwambiri ndi izo. Koma ndife Achimerika, mwaona, umo ndi mmene zikuyenera kukhalira. Mulungu anati tirigu ndi zoyanga ndi nansongole zikulire pamodzi. Musayesere kuti muzizule izo. Muzilole izo zikulire pamodzi, koma ndi zipatso zawo inu mudzawadziwa iwo. Palibepo zipatso, bwanji, palibepo Moyo, palibepo kalikonse pamenepo.

⁵⁵ Tsopano, tapenyani kakhungu aka. Tiyeni tinene, mwachitsanzo, monga nthawi zambiri, khansa yofiira kawirikawiri imakhudza mchiberekero cha mkazi, zovulala zachikazi ndi zina zotero. Tsopano zimenezo, tiyeni titenge zimenezo, mkulu ameneyo pamenepo tsopano, pa khungu lake, khansa iyi—iyi. Tsopano khansa . . .

⁵⁶ Chirichonse chathupi chimaimira chauzimu. Kodi inu mumadziwa zimenezo? Chirichonse chathupi chimaimira chauzimu, mulimonse.

⁵⁷ Mwachitsanzo, monga ichi, pamene—pamene ife tibadwa mu Thupi la Khristu, pali zinthu zitatu zimene zimakhlapo kuti zibweretse Kubadwa kwathu. Ndipo zimenezo ndi zinthu zitatu zimene zinatuluka kuchokera mmoyo wa Khristu pamene Iye anafa. Pamenepo panatuluka kuchokera mthupi Lake, madzi, Magazi, Mzimu. Nkulondola uko? [Osonkhana

akuti, “Kulondola.”—Mkonzi]. Zinthu zitatu, ndizo zinthu zimene ife timadutsamo pamene ife tikubadwa mwatsopano: kulungamitsidwa, kuyeretsedwa, ubatizo wa Mzimu Woyera. Tsopano, zimenezo zonsezo zikhoza kukhala mu kuchita kumodzi. Koma izo zimatengera...Koma inu mukhoza kukhala mu chikhalidwe cholungamitsidwa musanayeretsedwe. Inu mukhoza kukhulupirira pa Ambuye Yesu Khristu ndi kumanyamulabe nyansi zanu. Koma inu mwamtheradi mukhoza kumakhala mu ziwiri zonse kulungamitsidwa ndi moyo woyera wopatulika, ndipo wopanda Mzimu Woyera. Mwaona, Baibulo, Yohane Woyamba 5:7, anati, “Pali atatu amene amachitira umboni Kumwamba, Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera, ndipo...Atate, Mawu, ndi Mzimu Woyera,” amene anali Mwana, “ndipo zitatu izi ndi chimodzi. Ndipo pali zitatu zimene zimachitira umboni pa dziko lapansi, madzi, Magazi, ndi Mzimu, ndipo zimagwirizana mu chimodzi.” Osati chimodzi, koma zimagwirizana mwa chimodzi. Inu simungakhale ndi Atate wopanda kukhala ndi Mwana; inu simungakhale ndi Mwana wopanda kukhala ndi Mzimu Woyera, pakuti izo ndizosalekanitsika, mmodzi. Utatu uli mwa mmodzi.

⁵⁸ Ine sindimazimva izo mbali ya kuno, koma inu mumamva zochuluka kudutsa mdzikoli, chimodzi mwa zinthu zazikulu kwambiri mu magulu a Chipentekoste, ndi kusokonezeka mu chinthu chimodzi chophweka icho. Ndipo ine ndawasonkhanitsapo akuluakulu awo pamodzi ndi kuwatsimikizira iwo kuti awiri onsewo amakhulupirira chinthu chimodzi. Ndi mdierekezi pakati pawo, ndizo zonse. Ngati mpingo waukulu wa Chipentekoste uwo ungati u-... ungaponyere pansu zazing’ono izo, miyambo yakale ndi kudziyanjanitsa iwoeni pamodzi mu Mpingo wa Mulungu umodzi wodala, Mkwatulo ukhoza kubwera. Koma bola ngati Satana akuwaphwasula iwo, chabwino. Ndiyo njiya yake yochitira izo. Ndipo iwo mwamtheradi amakhulupirira chinthu chomwecho.

Wina amati, “Chabwino, *ichi* ndi Ichu.”

⁵⁹ Ine ndinati, “Chabwino, ngati *ichi* ndi Ichu, ndiye Ichu ndi *ichi*.” Chotero ndi inu apo. Chotero, chonsecho ndi chinthu chomwe chomwecho. Koma ndi zimenezotu, mu utatu wapatau umenewo wa Mulungu. Tsopano, tsopano, Mulungu mu umodzi Wake. Mulungu Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera. Tsopano, ife sitimanena kuti “milungu yathu,” ngati achikunja. Ndi “Mulungu wathu.” Mukuona? Ndi Umunthu wofutukuka patatu wa Mulungu.

⁶⁰ Tsopano zindikirani, tsopano, Satana ali mu utatu nayenso. Ndipo mphamvu zake ziri mu utatu.

⁶¹ Tsopano, koma zindikirani ndiye pamene madzi, Magazi ndi Mzimu zimabweretsa Kubadwa kwatsopano. Nkulondola

uko? Tsopano penyani. Ndi zimene zimaimirira Kubadwa kwatsopano. Nchiyani chimene chimaimirira kubadwa kwathupi Kubadwa mwatsopano kusanabwere? Pamene... Inu amayi, pamene mwana akubadwa, chinthu choyambirira ndi chiyani? Madzi. Chotsatira, magazi. Chotsatira, mwaona, zimenezo zimapanga moyo, mwaona, zimapanga munthu. Madzi, magazi, mzimu.

⁶² Tsopano, khansa, tiyeni tichite nayo kwa otsatira athu. Ife tiri ndi pafupifupi maminiti faivi omwe atsala, ine ndikuganiza. Pafupifupi mamitini faivi otsatira, tiyeni tichite nayo khansa. Kodi kamunthu kameneko ndi kandani? Kodi iye amaimirira khwangwala, amadya zinthu zakufa. Ndipo khansa imayambira pa kabala, kawirikawiri, pamene kakhungu kagundidwa ndipo iko—iko kasweka. Ndipo kakhungu kakang'ono mmenemo kamadzabwerera mmbuyo. Oh, amenewo ndi mawu aakulu kwa a Baptisti, sichoncho? Chabwino, koma iko kamabwerera mmbuyo, kakhungu kameneko. Ndine wa Baptisti amene ndimakhulupirira mu kubwerera mmbuyo.

⁶³ Winawake anati, kumusi kuno mu msonkhano waku Arkansas tsiku lina, anati, "M'bale Branham," anati... Anali mzanga wa Nazarene. Iye anali atachiritsidwa. Iye anali ndi zake... Amayendayenda mtawuni, ataika ndodo zake pa phewa pake. Iye anati, "Inu mukudziwa chiyani?" Anati, "Pamene ndinabwera kuno koyamba," anati "Ine—ine ndinkaganiza inu... ndinakumvani inu mukulalikira, ndinkaganiza kuti ndinu wa Nazarene." Iye anati, "Kenako ndinawona kuti anthu ambiri ndi a Pentekoste, ndipo winawake anandiuza ine kuti ndinu wa Pentekoste. Ndipo tsopano inu mukuti ndinu wa Baptisti." Anati, "Ine sindikuzimvetsa zimenezo."

⁶⁴ Ine ndinati, "Oh, izo ndi zophweka." Ine ndinati, "Ndine wa Pentekoste Nazarene Baptisti." Chotero uko—uko nkulondola. Chabwino. Ayi, ife ndi amodzi mwa Khristu Yesu, mwa Mzimu Woyera akutipanga ife kukhala mmodzi. Uko nkulondola.

⁶⁵ Tsopano, zindikirani, kakhungu kakang'ono aka kamabwerera mmbuyo iko kakavulazidwa. Kamayamba kakang'ono. Tizirombo tina timathamangirapo kuti tikakhale moyo pamenepo. Ndipo ndi momwe mafinya amabwerera pa chilonda. Timeneto timakhala asirikali aang'ono akumenyanirana moyo wanu. Ito timathamangira pamenepo ndipo—ndipo timaikapo chiphe chimenecho, mphamvu za ziwanda zimenezo zimene zimayesera—kuyesera kuti ziwunjikane pamenepo, ndi kupereka miyoyo yawo. Ndizo zimene zimapanga... Ndizo... Iwo ndi mulu wa asirikali pang'ono akufa, mafinya amenewo amene ali mmagazi mwanu... amene ali pa—pachironda, amene amapereka moyo wawo kuti apulumutse wanu.

⁶⁶ Tsopano, kakhungu kakang’ono kakangokana pamenepo ndiye chiwanda ichi chimayambapo, icho chimayamba kukula, icho chimayamba kuchulukitsa timakhungu. Icho chimakhala chikumanga thupi ndendende basi momwe ana anu amayambira mchiberekero mwanu, ndipo monga inu munachitira mwa amayi anu. Khungu pamwamba pa khungu, khungu pamwamba pa khungu, khungu, mulimonse, paliponse; basi, iwo amakhala opanda mawonekedwe a chirichonse monga munthu, monga mwa khalidwe lake. Icho chimangochokera mu mzimu. Icho chimangokula mulimonsemo, ndipo chimayamba khungu pamwamba pa khungu, khungu pamwamba pa khungu.

⁶⁷ Ndipo tsopano, chinthu choyamba inu mukudziwa, inu mumayamba kufooka ndipo mumadzimva kudwala. Inu mumapita kwa adokotala ndipo iye amakakupimani. Mwinamwake iye amalephera kuti apeze iyo. Ngati iye ayipeza, mwinamwake amaidulapo iyo. Ngati iye angakhoze kuidula bwino, chabwino, iye wathana nayo iyo. Koma ngati iye saidula iyo bwino, ndiye ngati iyo ili pa mmero kapena penapake pamene iyo singadulidwe bwino, kachidutswa kamodzi kakang’ono kakhilabe moyo. Mwaona, chifukwa siziri ngati kuti inu mukadula dzanja lanu ndiye kuti zathera pomwepo, kapena chirichonse, kapena mukalidulapo... Chimene ine ndikutanthauza, ngati inu mungadule thupi lathunthu, ndi kusiyapo dzanja lanu pamenepo, bwanji, iyo siingakhale moyo. Koma—koma, mwaona, iyo ilibe maonekedwe a moyo umene inu muli nawo. Iyo ndi mphamvu ya chiwanda ikuyenda.

⁶⁸ Ndipo tsopano zindikirani, inu mumazitchula izo, adokotala amazitchula izo, “khansa.” Mulungu amazitcha izo “mdierekezi.” Tayang’anani lero. Iwo angozipeza kumene izi... Kodi mawu akuti *khansa* anachokera kuti? Iwo amachokera ku... amachokera ku mawu a Chilatini amene amagwiritsidwa ntchito mu zachipatala, kutanthauza “nkhanu,” nkhanu imene inu mumaiwona mmphepete mwa nyanja, imakhala ndi miyendo yonse. Umo ndi momwe—momwe iyo imachitira, imadzitulutsa, imazimwaza. Mawu akuti khansa ndi nkhanu. Ndipo iyo imalowa ndipo imakhalabe itagwiritsitsa ndi kumayamwa magazi pamene iyo ikupita, monga nsundu kapena chinachake. Bwanji, chotupa, ng’ala, ndi nthenda zina, iliyonse ya izo imachokera ku nyongolosi, ndipo nyongolosi imeneyo imayenera kukhala thupi. Ndipo iko kasanakhale thupi, kamayenera kukhala moyo. Iko kasanalenge kapena—kapena kumera ndi kupanga timakhungu tochuluka, iko kamayenera kukhala moyo. Kulondola uko? [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi]. Tsopano, kodi khansa imeneyo inachokera kuti? Ndani, kodi iyo inachokera kuti? Iyo sinali pa inu apa nthawi yina yapitayo, koma tsopano mwina ili pa inu. Kodi iyo inachokera kuti? Ndi moyo wina wosiyana ndi moyo wanu, ukukhala mwa

inu. Ndipo ndi wozunza, kumayamwa moyo wanu. Ndi chifukwa chake Yesu anaitcha iyo “mdierekezi.”

⁶⁹ Lero iwo amati khunyu, iwo amati, “khunyu.” Bwanji, khunyu, mu Baibulo, Yesu analitcha ilo “mdierekezi.” Pamene bambo anabwera ndi mnyamata amene ankagwa pansu, ndipo ankatuluka thovu kukamwa, ndi chirichonse, iye anati, “Iye ali ndi chiwanda, ndipo nthawi zambiri chimamuponyera iye pa moto, mmadzi.”

⁷⁰ Tsopano iwo analipukuta dzina lake ndipo analitcha ilo khunyu, koma iye ndi mdierekezi. Ndipo Yesu anati, “Iwe mdierekezi, tuluka mwa mwanayo!” Ndendende. Tsopano, khunyu kawirikawiri limayamba kuchokera ku vuto la impyso. Mwinamwake inu mulowa mu zimenezo kanthawi pang’ono. Mukuona? Izo zimayambitsa khunyu, kuchokera ku kuundana kwa nkodzo.

⁷¹ Tsopano, zindikirani izi, ndiye kakhungu kameneko kamakhala pamenepo, ndi mdierekezi. Iye akumangapo moyo; iye akukula, akukulira kulira. Iye ali ndi ntchito imodzi yoti achite, ndiyo, kuchotsa moyo wanu. Ndicho chimene mdierekezi anamutumizira iye, kuti adzafupikitse masiku anu pa zaka sevente.

⁷² Tsopano, ine ndimalemekeza dokotala aliyense. Inde, bwana. Sayansi ya zamankhwala iliyonse, Mulungu awadalitse iwo chifukwa cha thandizo limene iwo awachitira anthu. Uko nkulondola. Inu mukanachita chiyani mdziko lero opanda iyo? Ine ndikumuthokoza Mulungu chifukwa cha sayansi ya zamankhwala. Ine ndikumuthokoza Mulungu chifukwa cha galimoto yanga. Ngati Mulungu akanapanda kulola sayansi kuti indipangire ine galimoto, ine ndikanakhala ndi nthawi yovuta yomayenda kubwera kuno. Chifukwa cha magetsi, ndi chifukwa cha sopo wosambira mmanja mwanga, ndi mankhwala a mmano okwechera mano anga, ndithudi. Ine ndikumuthokoza Iye chifukwa cha chirichonse, chifukwa zinthu zabwino zonse zimachokera kwa Mulungu.

⁷³ Koma ndiloleni ine ndikuuzeni inu, palibe chidutsa chimodzi cha mankhwala chimene chinayamba chachiritsapo nthenda iliyonse. Ndipo palibepo dokotala mmodzi, pokhapokha ngati alipo wabodza winawake, koma dokotala weniweni adzakuuzani inu kuti iwo samadzinenera kuti iwo ndi ochiritsa. Uko kwa a Mayo Brothers, ambiri a inu. . . Ine ndafunsidwapo mafunso kumeneko, kawiri kapena katatu. Za odwala amene amachokera kumeneko, osachiritsidwa. . . Inu munawerenga *Reader’s Digest*, ya mu Novembara? Ndi angati anawerenga ya mu Novembara, nkhani ya ine ija mmenemo, mu *Reader’s Digest*? Mukuona? Ndipo iwo anandiika ine mmenemo, zokambirana za khanda limene iwo anali atalilephera. Anati, “Izo sizikanatheka.” Koma Mzimu Woyera unayankhula ndi

ine ndipo unandiuza momwe izo zikanati zidzachitikire, ndipo izo zinachitika. Chabwino. Tsopano, iwo anandiitanitsa ine kumeneko. Ndipo pakhomo kumene pamene Jimmy ndi iwo, a Mayo ankakhala kumeneko, pali chikwangwani chachikulu chimati, “Ife sitimadzinenera kuti ndife ochiritsa. Ife timangodzinenera kuti timathandizira chirengedwe. Alipo mmodzi Mchiritsi, ameneyo ndi Mulungu.” Iwowo ndi omwe ali okhoza kwambiri ndzikoli. Tsopano, ife tiri nawo abodza apang’ono, inde. Uko nkulondola. Ife tiri nawo alaliki abodza, aponso. Chabwino. Chotero, izo zimapita mbali zonse ziwiri.

⁷⁴ Zindikirani, koma munthu aliyense yemwe amadzinenera kuti iye ndi mchiritsi, iye ndi wanthano, chifukwa iye sangathe kuchita zimenezo. Pakuti Baibulo linati, “Ine ndine Ambuye Amene ndimakhululukira machimo anu onse ndi kuchiza nthenda zanu zonse.”

⁷⁵ Ine ndakhalapo ku kafukufuku. Ndipo mchipinda changa, a... abweramo ena a madokotala apamwamba kudutsa mafuko. Inu simukudziwa kumbuyo kwa moyo, mzanga, kuti mudziwe zimene zakhalapo, ndi zinthu zimene ine sindimanena pagulu. Anthu amabwera mwamseri. Ndipo musaganize kuti palibepo a Nikodemo ochuluka mdziko; ndithudi alipo, masauzande a iwo. Iwo amayang’ana pa zimenezo ndipo amabwera mu msonkhano. Amadzakhala pamenepo atavala T-sheti, chinachake chimzake ngati chimenecho, ali ndi maina opukutidwa amene inu mukhoza kudabwitsidwa nawo, atakhala mu msonkhano kumene. Mu masiku pang’ono amazembapo ndipo amaimba mwamseri, ndi kumutumiza winawake kuti adzandifunse mafunso. Ndipo ndikunena pomwe pano, kuti, “M’bale Branham, ine ndikukhulupirira Icho ndi Choonadi.” Iwowo ndi anthu chimodzimodzi monga momwe ife tiri. Ndithudi. Ndipo munthu aliyense akukhumba kuti ayang’ane kudutsa chotchinga chakudacho uko komwe iye akuyenera kuti adzadutseko tsiku lina.

⁷⁶ Koma makhansa amenewo ndi zinthu izi ndizo mwamtheradi ziwanda zitaumbidwa mu thupi la mnofu, zikuyendayenda, kumatenga moyo wanu.

⁷⁷ Tsopano, ngati ine ndingachite ngati dokotala, ngati ine ndingayidulepo iyo, nkuisiya pansi... Kapena, monga ngati, tinene, mwachitsanzo, inu munali khansa, inumwini, pa dziko lino. Tsopano, awa ndi machiritso Auzimu. Ngati ine nditafuna kuti ndingothana nanu mwanjira ya adokotala, ine ndikhoza kumango... ndikhoza kungosisita thupi lanu, kapena chinachake chimzake, mpaka iyo yonse nkungosowapo pa dziko lapansi. Siingakhaleponso iliyonse ya iyo, chimodzimodzi monga adokotala amachotsera chotupa pa inu. Koma mmawonekedwe a machiritso Auzimu, ngati inu mukanakhala khansa, ine ndikanangoitana moyo wanu kuchokera mwa inu, ndipo inu mukanamapitirira. Moyo wanu ukanakuchokerani

inu, koma thupi lanu likanakhala pano basi chimodzimidzi monga ilo linaliri.

⁷⁸ Tsopano, pamene ndi pamene kupenya ndi nthawi ndi mdani woyipa wa Mulungu mu machiritso Auzimu. Ine sindikudziwa ngati M'bale Baxter amafikira kwa zinthu izi mu msonkhano. Ine ndinakhala pansi, ndinazifotokoza izo kwa iye ndi M'bale Bosworth, mobwerezabwereza. Koma apa pali chimene chimachitika. Ine ndikukaikira ngati anthu ambiri amazimvetsa izo, chifukwa, pakapita kanthawi, iwe umayamba kuwapeza anthu akubwereranso, akuti, “Ine ndinachiritsidwa, M'bale Branham, kwa masiku awiri kapena atatu, koma, Mulungu adalitsike, iwo—iwo andichokera ine.” Ndipo ine ndimazipeza izo, ndipo ine ndikuganiza kuti ndi chifukwa chakuti iwo samakhala mu msonkhano moyenera. Anthuwo samamvetsetsa. Ine ndakhalapo nawo anthu kubwera pa nsanja ndipo nkukhala akhungu kwathunthu, makhansa, kapena ng'ala mmaso mwawo, ndipo nkumawerenga Baibulo ili atatha kupemphereredwa, nkutsikapo; mmasiku atatu kapena foro nkukhalanso akhungu momwe iwo analiri poyamba. Chinachitika ndi chiyani? Aliyense amadziwa kuti pamene moyo watuluka mthupi lirilonse, iwo umafota kwa kanthawi. Nkulondola uko?

⁷⁹ Alipo aliyense, pano, amene anayamba waphapo mbawala, kapena ng'ombe, kapena chirichonse monga choncho? Ndithudi. Chabwino. Inu mukayiyeze iyo usikuuno, inu alenje kunja kuno, azimzanga a ine. Inu mudzaphe mbawala ndipo mudzaiyike iyo pa sikelo, mudzawauze anyamata momwe iyo ikulemelera. Mudzawone! Mmawa iyo idzakhala yopepuka mapaundi angapo kusiyana ndi mmene iyo inaliri. Pamene munthu afa, woika maliro, chinthu choyambirira, amachotsa mano ongoikirira kapena diso, chirichonse chimene chiripo pamene, amachichotsamo; chifukwa, izo zimafota, izo zimatulukamo chifukwa thupi la munthu limafota. Mnofu wina uliwonse umafota. Pamene moyo uchoka mu mnofu, iwo umayamba kutsika pansi, kumafota. Ilo limachita zimenezo kwa pafupifupi maora sevene-thuu. Ndipo kenako ilo limayamba kufufuma. Galu wamng'ono akagundidwa, kunja kuno pa msewu. Mumulole iye akhale pamene ndi dzuwa kwa masiku atatu, ndipo mudzawone chimene chimachitika. Iye amakhala galu wamkulu kuposa mmene iye analiri. Iye amafufuma. Nkulondola uko? [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi].

⁸⁰ Chabwino, ndicho chinthu chomwecho chimene chimachitika pamene chi—chiwanda chitulutsidwa mwa munthu wodwala. Masiku pang'ono oyambirira, “Oh, ine ndikumverera modabwitsa.” Kenako amayamba kumati, “Ine—ine ndadwalika kuposa mmene ine—kuposa mmene ine ndinaliri. Ine ndataya machiritso anga.” Motsimikiza basi momwe chikhulupiriro chinatulutsira icho, kusakhulupirira kumabwezeretsanso icho

kenanso. Pamene chikhulupiriro chapha icho, kusakhulupirira kumaukitsanso icho. Yesu anati, “Pamene mzimu woipa utuluka mwa munthu, iwo umakayendayenda ku malo owuma ndipo iwo umabwereranso ndi adierekezi ena seveni.” Ndipo ngati bambo wabwino wa mnyumba sakuima pamenepo kuti atetezere khomo limenelo, iye amalowa mkati momwemo. Ndipo bambo wabwino woyang’anira nyumba yanu ndi chikhulupiriro chanu. Amati, “Khala kutali!” Ndi zimenezotu.

⁸¹ Koma tsopano mumuwone wodwala amene wachiritsidwa, mwawamba, pokhapokha ngati chiri chozizwitsa chapamwamba. Zomwe, machiritso Auzimu ndi chozizwitsa ndi zinthu ziwiri zosiyana. Machiritso Auzimu, chinthu chinodzi; chozizwitsa ndi chinthu chinanso. Koma kuchita kwa wamba kwa machiritso Auzimu, pamene mzimu wonyansa watulutsidwa kunja, mdierekezi wa khansa, pamene iye amusiya munthu, “Oh!” Tsopano, kapena titenge chinachake kuti muwone zowonera zochuluka, ine ndinene kuti, ng’ala. Chimachitika ndi chiyani pamene munthu uja... Ngati inu mungamuzindikire munthu wakhungu. Ine sindikudziwa ngati ndinakhalapo naye aliyense kuno kapena ayi, panobe, wa maso a ng’ala. Ine ndimawalola iwo aimirire kwa maminiti angapo. Bwanji? Kuchitira kuti kufota kuja kuyambe kuchitika. Ndimawauza iwo kuti adzabwerere, adzatipatse ife umboni. “Oh, mai!” Iwo akukhoza kuwona modabwitsa. “Oh, mai! Basi, ine ndikukhoza kuwona zinthu! Inde! Ine...” Vuto ndi chiyani? Moyowo wachokamo; thupi la ng’ala likufota. Chabwino, izo zimatero kwa masiku angapo. Kuti, “Oh, ine ndikupeza bwino kwambiri.”

⁸² Ndipo pakapita kanthawi, iwo amayamba kumva kupweteka mutu, sakumva bwino kwenikweni. Amadzukapo mmawa wotsatira, “Sindikutha kuwonanso panonso.”

⁸³ Ena a iwo anati, “Uh-huh, iwe unangotengeka. Gulu la oyera odzigudubuzo ilo linangokupangitsa iwe kutengeka.” Iwe usamakhulupirire zimenezo! Limenelo ndi bodza la mdierekezi. Ngati iwe ungakhulupirire zimenezo, iwe umabwereranso kukhala wakhungu kenanso.

Koma ngati iwe unagawiritsitsebe, ndikuti, “Ayi. Ambuye, ine ndikukhulupirira.”

⁸⁴ Ndiye chimachitika ndi chiyani? Thupi limenelo limatupa kwa nthawi yaitali. Ilo limadzaphimbanso masowo. Khansa imeneyo mthupimo imafufuma. Iwe umayambanso kumamva kupweteka ndi kuwawa kenanso. Kenako iwe umadwalika kwambiri, kudwalika moyipa. Chifukwa chiyani? Chotupa chachikulu chija cha mnofu wakufa mwa iwe chiri pamenepo, chafa.

⁸⁵ Iwe ukabwerera, adokotala ndipo iye amati, “Oh, izo ndi zamkhutu. Khansayo ikadali pomwepo. Ine ndikukhoza

kuiwona iyo.” Ndithudi, iyo ili pamene, koma ndi yakufa. Aleluya!

⁸⁶ Tsopano, kuyenda kwa magazi kumayenera kuti kutsuke thupilo. Nthawi iliyonse imene mtima ukugunda, iwo umaponyera magazi kuzungulira mthupi, ndipo amanyamula nthenda imeneyo. Ndithudi, izo zimakudwalitsa iwe. Bwanji ngati mukanakhala ndi mulu wa nyama utapachikidwa mwa inu penapake, kapena yayitali ngati njoka, kapena chinachake chachikulu ngati chala chanu, ndipo chitapachikidwa mmenemo, ndipo chiri chakufa, nyama yakufa yochuluka chomwecho itapachikidwa mwa inu, ndipo iyo ikuvunda? Chabwino, ndithudi, kuyenda kwa magazi anu kukuyenera kuti kuziziyeretsa zimenezo, pamene iwo ukugunda. Koma apo pali thupi lakufa, chinthucho chikulendewera pamene, chifukwa chakuti moyo wachoka mwa icho. Mphamvu ya Mulungu, kudzera mu chikhulupiriro, inachitulutsapo icho. Iye ndi chiwanda; iye akuyenera kuti achokepo.

⁸⁷ Koma, chifukwa chake ndi chakuti, anthu samalangizidwa. Iwo amachokapo, amagonja. Ndipo mdierekezi yemweyo amaima pamene, kuti abwereranso kenanso. Pamene Mulungu akuuzani inu chirichonse pa nsanja pano, kudzera mwa Mzimu Wake, pamene ziri pansu pa kuzodza, musamakaikire chimenecho, kapena chinthu choyipa chidzabwera pa inu, Iye anatero. Pakuti Yesu anati, “Chikhaliidwe chotsirizira cha munthu ameneyo chinali choyipa kuchulukitsa ka seveni kuposa mmene zinaliri poyamba.” Nkulondola uko? Pamene mzimu woipa unatuluka mwa munthu, iwo unkayenda yenda mmalo owuma, unabwereranso ndi adierekezi ena seveni. Chotero, inu musamakhale osakhulupirira. Muzikhala kumene ndi Iwo. Muzitanthauza izo, kuchokera mu mtima mwanu. Muziti, “Ayi, bwana! Ine sindisunthidwa! Ziribe kanthu mmene ndingadwalire, izo sizikhala ndi kanthu kochita ndi izo.” Ndiye, chinthu choyambirira inu mukudziwa, inu mudzakhala mukupeza bwino. Chirichonse chidzakhala chabwino bwino pamene. Mwaona, icho chafa. O—oparesoni imene adokotala akanati akhale nayo pa inu, chotupa chomwecho chiri mwa inu, chopanda moyo mwa icho.

⁸⁸ Inu mukuti, “Moyo mwa icho, M’bale Branham, kodi izo zichotsa moyo wanga?” Ayi, bwana. Moyo umenewo ndi moyo wosiyana ndi wanu. Ine ndangokuwonetsani inu kumene kuti ndinu moyo ndipo mumakhala chinthu chamoyo, ndipo ndi moyo ndipo umadzakhala chinthu cha moyo; ndipo ndinu wa Mulungu, ndipo iwo ndi wa mdierekezi. Inu mukuwona chimene ine ndikutanthauza? Phunziro La Ziwanda. Tsopano, inu mukuyenera kuwona momwe chinthu chimenecho chimawonekera pamene inu muyima ndi kuyang’ana pa icho.

⁸⁹ Oh, mai, ine ndikupepesa, ndi pafupifupi hafu firii. Ine ndikupepesa. Taonani, amzanga. Oh, chimene dziko ili likusowequera!

⁹⁰ Ine ndakhala pafupifupi zaka seveni, ndikuphunzitsa kudutsa Amerika, ndikukhala ndi misonkhano ya machiritso iyi. Ine ndinangokhala ndi ganizo labwino loyamba kubwerera kudutsa mdzikoli, kuphunzitsa Baibulo, ndi za phunziro la ziwanda, momwe anthu angamvetsere zimene akuyenera kuchita. Ndipo ndi chifukwa chimene, iwo amapita ku misonkhano iyi, nthawi zambiri, ndipo, munthu... Ngati simukumvetsa, anthu amachokapo, ndipo nthawi zambiri...

Tsopano, kumbukirani munthu uja amene amabwera ndipo nkuti anali ndi mphatso ya machiritso Auzimu? Mphatso ya machiritso Auzimu inali mwa inu ngati inu munachiritsidwa. Ndi inuyo, pamenepo. Mphatso iliyonse imagwira ntchito mwa chikhulupiriro. Ndipo ziribe kanthu kuti ine ndiri ndi mphatso ya machiritso Auzimu yochuluka bwanji, ine ndimakhulupirira izo ndi mtima wanga wonse, koma iwe ukhoza kuyima apa ndipo, ngati iwe ulibe mtundu womwewo wa chikhulupiriro, izo sizimakuchitira iwe ubwino. Ine ndikhoza kukupemphererani inu, kwa maora ndi masabata ndi miyezi. Si alaliki amene amakhala ndi machiritso Auzimu. Ndi inuyo amene mumakhala ndi mphatso ya machiritso Auzimu, amene mumakhulupirira za kuchiritsidwa, chifukwa ndi mwa chikhulupiriro. Mwa chikhulupiriro! Chochitika chirichonse cha Mulungu chimakhala mwa chikhulupiriro.

⁹¹ Zida zonse za Mulungu ndi za mwachikhulupiriro. Ife tiribe chinthu chimodzi chachirengedwe cha dziko lino. Chirichonse cha—cha mpingo Wachikhristu ndi kachitidwe ka chikhulupiriro. Tayang'anani pa zida za Mulungu, chikondi, chimwemwe, mtendere, kulezamtima, ubwino, kudzichepetsa, chifatso, chipiriro. Nkulondola uko? Chirichonse chazimu, palibepo chathupi. Chotero ife sitimayang'ana pa zinthu mwathupi, chifukwa tikuchita mwauzimu. Ndipo njira yokhayo imene ife tingazikhazikitsirepo izo, ndi chikhulupiriro, pa chimene Mulungu ananena kuti ndi Choonadi, ndipo ife timayang'ana pa Chosawoneka. Ndipo ife timadzitcha zinthu zimenezo zimene palibepo, ngati kuti zinalipo; monga Abrahamu anachitira, ndipo anachipeza icho. Amen! Abrahamu anadzitcha zinthu zimenezo zimene kunalibe, monga Mulungu anachitira, ngati kuti zinalipo. Pokhala wa usinkhu wa zaka handirede, sanadzandime pa lonjezo la Mulungu kudzera mu kusakhulupirira.

⁹² Ine ndikhoza kungoganizira zimenezo, inu simungatero? Kumuwona Sarah akudzuka mmawa wina. Mulungu anati, "Abrahamu!" Anati, "Abrahamu, iwe udzakhala ndi mwana."

⁹³ Sarah anadzuka. Anati, “Ukupeza bwanji, Sarah?” Ili ndi gulu losakanikirana, koma mvetserani.

“Palibe kusintha.”

⁹⁴ “Chabwino, ulemelero kwa Mulungu, ife tidzakhala naye! Pita ukatenge matewera ndi maphinifolo, ndi chirichonse. Ukonzekere.”

Chabwino, mwezi wina unadutsa. “Sarah, ukumverera bwanji?”

“Palibe kusintha.”

Chaka chinadutsa. “Sarah, nanga bwanji izo?”

“Palibe kusintha.”

Zaka teni zinadutsa. “Palibe kusintha.”

Zaka twente-faivi zinadutsa. “Palibe kusintha.”

⁹⁵ Abrahamu, mmalo momafooka, iye ankakhala wamphamvu ndi wamphamvu. Iye ankadziwa kuti chidzakhala chozizwitsa chachikulu nthawi yonseyo, chifukwa iye ankakhulupirira Mulungu, ndipo sanadzandime pa lonjezo la Mulungu kudzera mu kusakhulupirira. Iye anati, “Ife tidzakhala naye iye!” Ndipo mmawa wina chiberekero cha Sarah chinayamba kufufuma, ndipo Isaki wamng’ono anadzabadwa, chifukwa chakuti Abrahamu anakhulupirira Mulungu. Ndipo iye anayang’ana pa zinthuzo, ndipo anaziwerengera zinthu zimene panalibepo ngati kuti zinalipo.

⁹⁶ Osati mwa zomverera, osati mwa kupenya. Inu simumayenda ndi zomverera ndi kupenya. Ndi mwa chikhulupiriro. Ndipo Mulungu akayankhula chinachake, akati, “Zinthu zirizonse zimene inu mupempha, pamene mupemphera, mukhulupirire kuti mwalandira izo,” zikatero mugwiritsitse kwa izo. Mulungu watero, zikuyenera kukhala chomwecho! Ameni. Ziwanda!

Chikhulupiriro mwa Atate, chikhulupiriro
mwa Mwana,
Chikhulupiriro mwa Mzimu Woyera, atatu awa
ndi Mmodzi;
Ziwanda zimanjenjemera ndipo ochimwa
amadzuka;
Chikhulupiriro mwa Yehova chimagwedeza
chirichonse.

Uko nkulondola. Oh, mai! Ndithudi ndi choncho. Khalani ndi chikhulupiriro mwa Mulungu. Muziyang’ana kwa Iye. Inu musati musunthepo. Mukhale pomwepo. Mulungu ananena chomwecho!

⁹⁷ Ndipo, ziwanda, izo ndi chiyani? Izo ndi zinthu zauzimu. Tsopano, a—dokotala amati, “Inu muli ndi khansa. Inu muli ndi TB. Inu muli ndi ng’ala. Inu muli ndi kutupa kwa mapapo. Inu muli ndi *ichi*.” Ameneyo ndi mdierekezi. Iwo ndi moyo, ndipo

kuseri kwa moyo umenewo kuli mzimu. Ndi angati amadziwa ndipo akhoza kuwona kuti khansa imeneyo, ng’ala, iyo ili—iyo ili. . . Iyo ndi mzimu, uli—uli ndi moyo mwa iyo. Chabwino, palibe chinthu chimene chingakhale ndi moyo popanda mzimu, mwaona, chotero pakuyenera kukhala moyo kuti uzichita zimenezo, penapake.

⁹⁸ Ngakhale mtengo uwo apo uli ndi moyo mkati mwake. Sayansi yonse pa dziko lapansi siingathe kupanga tsamba limodzi la udzu. Kodi inu mumadziwa zimenezo? Iwo amapanga chinachake chowoneka ngati ilo, koma iwo amalephera kuti apeze kapangidwe ka moyo. Ameneyo ndi Mulungu. Mukuona? Yesu ananena kwa mtengo, “Iwe ndi wotembereredwa. Iwe ulibe chipatso chirichonse, ndipo iwe sudzakhala nacho chirichonse.” Iwo anadzadutsanso pamenepo. Munali cha mma eyiti koloko mmawa umenewo. Anadzadutsaponso cha mma leveni koloko, pamene iwo ankapita kokadya chakudya chamadzulo. Petro anati, “Taonani mtengo uja, iwo wafa kuchokera ku mizu mpaka pamwamba.” Bwanji? Yesu anadzudzula moyo umene unali mu mtengo umenewo, umene unali ku mizu, ndipo chinthu chonsecho chinafa. Aleluya!

⁹⁹ Khristu yemweyo akhoza kudzudzula khansa kuchokera ku mizu, ndipo chinthu chonsecho chifapo. Mtengo umenewo unali utayima pamenepo chimodzimodzi basi mmene iwo unaliri, maora apambuyo, koma inu mukupeza kuti masamba anayamba kuthothokapo, ndipo kenako nkuwona chikhungwa chikusendekapo. Ndipo a. . . Unayamba kusasukapo, tsiku ndi tsiku, ndi sabata ndi sabata, ndipo patapita kanthawi panalibepo ngakhale chidutswa chimodzi cha mtengowo chinatsalirapo. Aleluya! Khansa, chotupa, ng’ala, kapena chirichonsecho, chikuyenera kuchokapo Khristu akayankhula. Iye amatulutsa ziwanda. Ndipo Iye anati, “Mu Dzina Langa iwo adzatulutsa ziwanda, adzayankhula ndi malirime atsopano, adzatola njoka, kapena adzamwa zinthu zakupha, izo sizidzawapweteka iwo. Ngati iwo adzaika manja awo pa odwala, iwo adzachira.”

¹⁰⁰ Inu mumamukonda Iye? Ine ndikupepesa ndakusungani inu kwa ora pano masana ano, mutakhala pano. Inu mumawakonda Ambuye? [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi]. Chitachitike ndi chiyani tsopano? Ngati inu mutamulandira Khristu ngati mchiritsi wanu, ndi kukhulupirira mu mtima mwanu kuti chinachake chachitika kwa inu, ndipo inu nkukhulupirira kuti mwachiritsidwa, kodi inu mukhulupirira kuti mwachiritsidwa? Musalole mdierekezi azike chirichonse pa inu. Muzingopitirirabe.

“Adokotala,” akati—akati, “adokotala, zikuwoneka bwanji?”

Iye akati, “Bwanji, iyo ili pomwepobe.”

¹⁰¹ Mu mtima mwanu inu mukudziwa, mukudziwa chimene chinachitika. Huh! Chinthu choyambirira inu mukudziwa, munene kuti, “Kuti, ndikudabwa chimene chachitika ndi chinthu chimenecho?”

¹⁰² Kenako mudzati, “Taonani, adokotala, ine ndikuuzani inu. Chachitika ndi ichi, Yesu Khristu wandichiritsa ine. Uko nkulondola. Yesu Khristu anandichiritsa ine.”

¹⁰³ Chabwino, tiyeni tiweramitse mitu yathu mphindi chabe. M’bale Willett, mungabwere kuno miniti chabe, m’bale?

¹⁰⁴ Tsopano, Atate Akumwamba, ndife othokoza chifukwa cha Magazi a Khristu. Ndipo mwinamwake nthawizina wantchito Wanu, Ambuye, samagwiritsa ntchito chidziwitso, poyankhula nthawi yotalika kwambiri. Koma ine mwinamwake ndikumverera ngati Paulo, amene analalikira usiku wonse usiku wina. Mnyamata anagwa kuchokera pa zenera ndipo anafa. Ndipo mtumwi ameneyo, ali ndi Mawu a Mulungu mmoyo mwake, anapita ndipo anakayika thupi lake pa mnyamatayo, moyo unabwerera mwa iye ndipo iye anakhalanso moyo.

¹⁰⁵ Wokonedwa Mulungu, ndikudziwa kuti kulowa dzuwa kwa chitukuko chapamwamba ichi tsopano kukulowa, chapita kwambiri, pakati pa tsiku padutsa, mithunzi ya usiku ikugwa. Kuwala kwakukulu kukubwerapo kuchokera ku Ufumu wa Mulungu, kuti kudzatenge malo ake a mdima waukulu uwu umene ukubwera pa dziko lapansi. Mulungu, ine ndikuzindikira kuti ndikukalamba tsiku lililonse. Ndiloleni ndizipita, Ambuye. Ndipatseni ine mphamvu. Ndithandizeni ine kuti ndizinenena Choonadi chachikulu ichi kulikonse. Mudzatithandize ife, mawa masana, kuti ife tidzamvetse mochuluka.

¹⁰⁶ Ndipo, wokonedwa Mulungu, dalitsani omvetsera ochepa awa masana ano. Usikuuno, pamene iwo asonkhanira msonkhano wa machiritso, mulole mwamuna aliyense ndi mkazi aliyense afikire kwa wina ndi mzake ndipo ayambe kukambirana, ndi kumati, “Tsopano, apa pali...musati—musakhalenso ndi kukaika kulikonse. Ife tikumvetsa kumene izo zikuchokera tsopano. Ife tikudziwa ndi mdierekezi. Ndipo ife tikudziwa kuti iye akachoka, iye akuyenera kubwera pa kulamulira kwa Mulungu. Iye akuyenera kutero. Mulungu ananena kale zimenezi. Iye akuyenera kuchokapo.” Ndiye, muwalole iwo atuluke, osangalala, akukondwerera, akutenga machiritso awo. Palibe chirichonse, musalole chirichonse kuti chiyime pa njira yawo, kenanso; angopita, akukhulupirira.

¹⁰⁷ Ndipo, Mulungu, mulole mpingo waung’ono uwu apa, ndi mipingo yogwirizana nawo iyi, ikhale ndi chitsitsimutso ukatha msonkhano uwu, Ambuye, chimene chitautengere iwo monsemo, ndipo mahandiredi a miyoyo ibweretsedwe mu Ufumu wa Mulungu. Perekani izi, Atate. Mulole amuna ndi akazi

pano, ochokera mmafuko ndi malo ena, mulole iwo atengere Uthenga kupita nawo ku mipingo yawo, ndipo mulole iwo akakhale ndi chitsitsimutso chachikale. Perekani izi, Ambuye. Tikhululukireni ife machimo athu tsopano. Mutithandize ife kuti tikhale antchito Anu. Mu Dzina la Yesu Khristu. Amen.

¹⁰⁸ Ine ndikudabwa, pamene inu mwakhala pano, alipo wochimwa mnyumbayi lero, amene angati, “M’bale Branham, mundikumbukire ine mu pemphero?” Inu mungatero, inu mungakweze mmwamba dzanja lanu? Alipo munthu wochimwa? Ine sindi. . . Mulungu akudalitse iwe, dona. Kodi alipo? Mulungu akudalitseni inu, bwana. Iwe, ndi iwe, ndi iwe, Mulungu akudalitse iwe. Ine ndikudabwa ngati inu. . . Tsopano, izi ziri ndi inu.

¹⁰⁹ Mwaona, ine sindikhulupirira zomapita mwa omvetsera. Ine sindikuwatsutsa ena amene amachita izo. Ine sindikhulupirira zomapita mwa omvetsera ndi kukayesera kumukoka winawake. Mukuona? “Palibe munthu amene angabwere, pokhapokha Atate Amene amamukoka iye.” Mukuona? Uko nkulondola. Inu mumangomukokapo iye pamenepo motsutsana ndi chifuniro chake. Mukuona? Koma ngati Mulungu akugogoda pa mtima wanu, ndinu munthu wamwayi waukulu mu dziko lapansi. Inu simukudziwa basi kuti ndi anthu angati amene ine ndayankhulana nawo.



PHUNZIRO LA ZIWANDA — DERA LATHUPI CHA53-0608A
(Demonology — Physical Realm)
MAULIKI A PHUNZIRO LA ZIWANDA

Uthenga uwu wa M'bale William Marrion Branham, woperekedwa mu Chingerezi Lolemba madzulo, Juni 8, 1953, ku Roberts Park Amphitheater mu Connersville, Indiana, U.S.A., unatengedwa kuchokera pa matepi ojambulidwa ndi maginito nudindidwa mosachotsera mawu ena mu Chingerezi. Kumasulira kwa Chichewa uku kunadindidwa ndi kugawidwa ndi Voice Of God Recordings.

CHICHEWA

©2021 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org

Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. Box 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org